Pemphero ndi Kusala kudya–Zothandizira Chitsitsimutso Cha Chiyero.

Vesi: Yoweli 2: 12-17

Uthengawu ukuonetsera kuti chitsitsimutso cha chiyero chimachokera kwa Mulungu potsatira pa pemphero loona mtima ndi kusala koyenera pakati pa anthu Ake. Izi ziyenera kulimbikitsa A Nazarene onse muno mu Afilika kuti adzipereke posala kudya ndi kupemphera.

Dziwani izi: Mlaliki ayenera kukhazikitsa cholinga cha ulalikiwu monga maziko a uthengawu.

Kuyamba Phunziro:

Mlili wadzombe ndi njala udaononga Yerusalemu ndi Yuda. Mneneri Yoweli akuona kuti ili ndi vuto ladziko lonse pokhudzana ndi tsiku lalikulu la Ambuye." (Yoweli 2:31). Pakati pa zovuta, mneneri akufuna kuti aliyense alape: mwana kapenanso wamkulu (1:2–3), oledzera (1:5), alimi (1:11) ndi ansembe (1:13). Dzombe limaimira ngati khamu la asilikali a Yehova ponena zatsiku lalikulu lachiweruzo cha Mulungu limene Ayuda osakhulupirika adzaweruzidwa. Koma mneneri akusimba kuti ngati anthu alapa, Israyeli adzakhululukidwa machimo ake.

1. **Uchimo Umaitana Chilango Nthawi Zonse:**
   a. Anthu a ku Yuda adamufulatira Mulungu wawo:
      1) Mulungu akuwaitana kuti alape (2:12,13).
      2) Iwo adali mtulo tauzimu naiwala kudziteteza mmoyo wawo wauzimu (1:3).
      3) Iwo adakonda maidyaidya kuposa kutumikira Mulungu.
         a) Iwo adatchedwa kuti anthu akumwa ndi kuledzera vinyo" (1:3).
         b) Iwo adakonda manyado koposa kusangalatsa Mlengi wawo.
   b. Mulungu adabweretsa chiweruzo pa Yuda ndi Yerusalemu chifukwa chakusakhulupirika kwawo:
      1) Mulungu atumiza khamu ladzombe kukaononga nthaka yawo (2:11).
      2) Chakudya chawo chidaonongeka ndikusiya kupezeka (1:16, 17).
      3) Chimwemwe komanso kukondwa kwa Nyumba ya Ambuye kudachoka pakati pawo (1:16).
      4) Kupezeka kwa madzi kudasokonezeka (1:20.)
   c. Chiweruzo chimatsatira uchimo:
      1) Lamulo la chipangano chakale la mdalitso ndi temberero (Deuteronomo 11:26-28).
      2) Lamulo lachipangano chatsopano la uchimo ndi imfa (Aroma 6:23).
   d. Kuonetsera kwa uchimo ndi chiweruzo:
      1) Zitsanzo za chiweruzo cha Mulungu pakati pathu masiku ano.
      2) Zitsanzo za uchimo umene ukupezeka mumpingo komanso mdera lathu masiku ano.

         (Mbusa ayenera kupereka zitsanzo za uchimo koma osanena munthu kapena zina zochitika).

3) Kusowa kwa ulemerero wa Mulungu mumpingo.

e. Chenjezo langozi yaikulu ngati anthu sathana ndi uchimo moyenera.

2. Kuitanidwa Kukulapa Kudzera Mukupemphera ndi Kusala Kudya (2:12–17)

a. Kulapa kwa Anthu amdera:

1) Bwererani kwa Ine ndi mtima wanu wonse (2:12, 13).

2) Kulapa kuyenera kuchokera mkati mwa mtima woona osati kunja chabe. "Ng'ambani mtima wanu osati zovala zanu (2:13).

a) Mlaliki apereke zitsanzo zakulapa kwa kunja kwa mtima ndikufotokozera mmene ndimeyi ikutsutsaniratu ndi kulapa kotere.

b. Pemphero la mdera

1) Kulilira kwa Ambuye (1:14).

2) Kudzanso kwa Ambuye ndi mtima wanu wonse: (1:12).

3) Kuitana ku mamasulidwe - "...pulumutsani anthu anu Ambuye." (2:17).

4) Kulunzanitsa anthu mpemphero lopempha chisomo ndikupezeka kwa Ambuye

a) kuitana msonkhano woyera (1:14;2:15,16)

b) kuitana akulu akulu ndi onse okhala mdziko (1:14).

c) kuphatikiza Ana ndi Iwo amene alowa mbanja kumene (2:16).

5) Pemphero lidzikhala lofunafuna nkhope ya Ambuye osati kudzionetsera chabe (Mateyu 6:1-14).

c. Kusala kwa Anthu amdera lonse

1) Ombani lipenga mziyoni ndikulengeza zakusala koyenera (1:14; 2:15).

2) Muyenera kuzindikira kuti langizo la Buku Lopatulika apa ndi kupemphera ndi kusala koyenera kwa anthu onse. Mutsindike kuti mavesi amene aperekedwa mmwambawa, akupempha kuti dera lonse liyenera kusalanso ndi kupemphera kwa Mulungu.

3) Kusala (kumene kutsagana ndi mtima wosweka) ndichizindikiro cha kudzichepetsa komanso kudalira Ambuye Mulungu kwathunthu. (Mateyu 6:16-18).

3. Kuyankha Kwa Mulungu ku Kusala Kudya ndi Kupemphera Koona

a. Mulungu amachotsa temberero ndi kuika mdalitso (2:13ndi 2 mbiri 7).

b. Mulungu amakhala ndi nsanje yabwino ndi kueteteza Anthu Ake (2:18, 25).

c. Mulungu amakumana ndi zosowa za Anthu Ake amene Afika kwa Iye (2:19, 26).

d. Mulungu amapezeka pakati pa Anthu Ake (2:28-32; 3:21).

e. Taonani mmene mavesi awa amayambira 2:12 ndi 3:28 akuyambira.

1) 2:12 - "Ngakhale tsopano" (lapani, salani ndipo pempherani tsopano)

2) 3:28 - "Ndipo pamapeto pake" (pamapeto pake ndidzatsanula Mzimu wanga)

3) Mulungu walonjeza kuti ngati timfuna ndi mtima wathu wonse, Iye adzapezeka (Mateyu 5:6, 7; Luka 11:5-13).

f. Taonani kuti Petro akunenanso za vesi iyi patsiku la pentekoste, kunena kuti zimene zidachitika patsiku la pentekoste, zidaloseledwa kale ndi mneneri Yoweli 2:28-32 (onani Machitidwe 2:16-21).

   1) Mneneri Yoweli adanena za Mulungu kutsanula Mzimu wake pa Ife ngati titapempherera ndikusala kudya moyenera ndi moona mtima.

   2) Mtumwi Petro akumangirira lonjezo la Mneneri Yoweli ku Chipangano Chatsopano pa zomwe zidachitika pa tsiku la Pentekoste.

4. Kugwiritsa Uthengawu Lero Mumpingo Wathu mu Afirika muno

a. Cholinga chathu mu Afirika muno ngati mpingo, komanso masomphenya athu, ndikumva kutsitsimuka koyenera aliyense payekha komanso mpingo wonse wa Nazarene (kufika kwa Mzimu wake pa ife tonse).

b. Dera lathu lampingo ku Afirika kuno likukakamizika pa zakutsitsimuka pa chiyero

c. Zolinga zathu ziyenera kulimbikitsa kutsitsimuka pa chiyero.

d. Chosowa chathu mu Afirika muno ngati mpingo ndi kutsanulilidwa kwa mpamvu ya Mzimu Woyera mumpingo wathu.

Kutsiriza:

Mmipingo yathu yonse muno mu Afirika anthu onse akupemphedwa kukhala ndi pemphero lakusala kudya ndi kupemphera kuti machimo athu akhulukukidwe komanso kuti Mzimu wa Mulungu utsike pampingo ndi mmadera athu.

Panyengo yonse ya Lenti ndi masautso a Ambuye wathu Yesu Khristu, lachitatu pa, 22 February 2012 mpaka Lamulungu loyera pa, 08 April 2012, A Nazarene onse adzakhala ndi nthawi ya kupemphera ndi kusala kudya.

Tikhala ndi nthawi yapadera imene pakhala maphunziro akusala kudya ndi kupemphera ndipo a Nazarene onse adzakhala pamodzi pogawana zakudya atatha kusala komanso adzakhala ndi nthawi yopemphera limodzi kuti pakhale kutsitsimuka pachiyero mu Afilika muno mumpingo wa Nazarene. (Gwiritsani ntchito mlozo wa pemphero ndi kusala kudya komanso kalendala ya pemphero pozindikira malo, anthu komanso zosowa zimene mutazipempherere pokhudzana ndi kupemphera komanso kusala kudya.)

Funsani mpingo, kodi ndinu okonzeka kupempherera komanso kusalira kudya inu nomwe, banja lanu, dziko lanu, dera lanu la afilika dziko lonse komanso anthu athu?

Mneneri Yoweli wachipangano chakale komanso mtumwi Petro wachipangano chatsopano onsewa akufuula kwa Ife lero ndi kuti: "Mfuneni Ambuye ndi mtima woona kudzera mkusala kudya ndi kupemphera ndipo adzatsanula mzimu wake lero muno mu Afilika komanso dziko lonse alapansi!

Langizo kwa Mbusa: Limbikitsani mpingo wonse kusala kudya ndikupemphera kwa masiku atatu. Mukhazikitse masikuwa nthawi yabwino ndikuwalengeza munthawi yabwino.

- Iwo amene sakudwala, ayenera kusala zakumwa ndi zakudya kwa masiku atatu koma ayenera kumwa madzi kwa masiku atatu.
- Iwo amene akudwala angathe kuyesera kusala pang'ono koma angathe kumadya kuti asafooke kwambiri ndi matenda awo.

By Rev Howie Shute

Ndipo Anthu Anga

Mawu Owerenga: 2 Mbiri 7:11-16

Vesi loloweza: 2 Mbiri 7:14

Chiyambi:

Uthengawu ukusonyeza kufunika kopereka nsembe pokhudzika ndi zinthu zimene zili zofunika pamoyo wathu. Timachita chilichonse kuti tipeze zimene tikuzikonda. Ifenso tiyenera kuyesetsa podzipereka kuti tipeze zinthu zofunikira kuchokera kwa Mulungu wathu? Uthengawu utisonyeza kufunika kwa chitsitsimutso ndikusamalitsa zotithandiza kuti mpingo utsitsimuke lero lino. Ndizachidziwikire kuti pemphero lakusala kudya ndikupemphera ndi lomwe lingachititse kuti Mulungu apezeke mumpigo komanso mdera lathu ndi padziko lonse lapansi.

1. **Kutsekulira Chitsanzo**

   a. Perekani chitsanzo chamoyo watsiku ndi tsiku pa zimene mumakhudzika nazo. Izi zidzakuthandizani ndi uthenga walero.

      Chitsanzo:

      Ndili ku sekondale sukulu ina ku Amerika, ndimakonda masewero ena ampira, masewerawa amakonda kusewera ndi amwenye amene akhalitsa ku Amerika. Chidali chinthu chofunika mmoyo mwanga. Ndinkafuna kukhala katswiri wapamasewerowa. Ngakhale kunyumba ndidali ndi zipangizo zothandiza kukonzekera bwino kuti ndidzipambana nthawi zonse. Anthu ena ankafuna kuti ndidziwaphunzitsa masewerowa koma ine ndimakhala kunyumba kukonzekeranso kuti ndichite bwino. Ndimatha kuthawanso maphunziro chifukwa chamasewerowa pamene anzanga ali mkalasi. Ndimalola kuti nditaye mwayi wamaphunziro kuti ndikhale wosewera wabwino. Iyi ndi nsembe imene ndimachita. Ndidaika mtima wanga kwambiri pamasewero.

      Mulungu adandikumbutsa mmene ndinkakondera masewera a Lacrosse mmoyo wanga ndipo adandikumbutsa kuti ndimkonde Mulungu koposa masewerowa. Mulungu adandifunsa kuti ndi nsembe yotani ungapereke kusonyeza kukonda Ine ndi mpingo wanga kuti mphamvu ya Mulungu iyende?"

   b. Limbikitsani Mpingo:

      1) Ganizani pachinthu chimene Iwo amachikonda zedi ndipo ndi nsembe yotani ayenera kuchita posiya zimenezi posonyeza kukonda Mulungu;

      2) Funsani funsoli: "Kodi mwakonzeka kuchita chiyani kuti muone chitsitsimutso mmoyo mwanu komanso mumpingo?"

      3) Pa 2 Mbiri 7:14 Mulungu watipatsa ndondomeko ya chitsitsimutso. Tiyeni tifufuze za cholinga cha ndimeyi imene ikunena zachitsitsimutso cha Mulungu komanso mmene chingapezekere pakati pathu:

   a. Mfumu Solomo adali atatsiliza kumanga kachisi wa Mulungu.

      1) Iye adali ndi zokongoletsa kachisi pamalo opatulika a Mulungu.

      2) Potsiliza, likasa la Mulungu lidaikidwa mukachisi.

      3) Ulemerero wa Mulungu udazinga kachisi wake.

         a) Ansembe sakadatha kupita mukachisi chifukwa ulemerero wa Mulungu udakukuma mwamphamvu (2 Mbiri 5:13-14).

b) Ichi ndi chosowa chachikulu champingo lero lino, kuti ulemerero wa Mulungu uzinge mumitima ndi mipingo yathu).

b. Solomo akupemphera pemphero la kupatulira kachisi kwa Ambuye Mulungu 2 Mbiri 6.

1) Solomo akuvomera kuti ana a Israyeli adzachimwa.

2) Solomo akupemphera kuti Mulungu adzakhulukira tchimo pamene a Israyeli atalapadi.

3) Solomo atatha kupemphera moto udatsika kumwamba ndikupsereza nsembe ndipo ulemerero udadzala mkachisi.

4) Mnazarene aliyense apemphere kuti ulemerero wakumwamba utsike pampingo wake ndi mmitima yathu kuti titsitsimukenso.

Dziwani izi: Mukhale ndi nthawi yowauza anthu zakufunika kwa chitsitsimutso mumpingo ndi pakati pa anthu. Alimbiktseni kufunafuna nkhope ya Ambuye ndi ulemerero wake.

c. Mulungu adamuyankha Solomo ndikukhulukira tchimo la anthu amtundu wake ndikubwezeretsanso Dziko Lake. Monga tilinso ndi chosowa ichi lero tiyeni tilape ndi kumvetsera kwa Mulungu.

3. Lonjezo Lachitsitsimutso:

a. Ndondomeko yachitsitsumutso: pamene Mulungu adaonekera kwa Solomo madzulo, Solomo adapatsidwa ndondomeko iyi:"ndipo anthu anga ochedwa padzina langa akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zawo zoipa; pamenepo ndidzamvera mmwamba, ndikukhulukira choipa chawo, ndikuchiritsa dziko lawo."

1) Lonjezoli lidapita kwa Israyeli, Ana a Mulungu. Komabe, lero lino, Ana a Mulungu ndi mpingo wa Yesu Khristu. Iwo otchedwa dzina lake ndi Akhristu. Lonjezoli ndilofunikanso lero kuposa masiku amake dzana.

2) Mau akuti **“NDIPO”** ndi ofunika kuwamvetsa palonjezoli.

a) Ngati tidya zakudya zochepa komanso kuchita masewro olimbitsa thupi ndiye kuti sikelo idzasika.
Koma ngati tidya zamagulu asanu ndi limodzi (6) ndikuchitanso masewro olimbitsa thupi ndiye kuti matupi athu adzakhala amphamvu ndi athanzi komanso ofewa.

b) Ngati tibzala mbewu nthawi yake ndipo mvula ikabwera, ndiye kuti tidzakhala ndi kholola wamphamvu komanso wochuruka.
Koma ngati sitidzala mbewu panthawi yake mvulanso ndikusabwera ndiye kui palibe chimene tingakolole.

c) Izinso zili chimodzimodzi pano. Ngati tichita mbali yathu, Mulungunso adzachita mbali yake,
Koma ngati sitichita mbali yathu, Mulungunso sadzachita mbali yake.

"ndipo anthu anga ochedwa padzina langa akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zawo zoipa; pamenepo ndidzamvera mmwamba, ndikukhulukira choipa chawo, ndikuchiritsa dziko lawo."

b. Mbali Ya Mulungu–LONJEZO LA KUTSITSIMUKA.

1) Iye adzamva mapemphero athu.

2) Iye adzakhululukira zochimwa zathu.

3) Iye adzachiritsa dziko lathu (dera, dziko, mpingo).

4) Ili ndi lonjezo la Mulungu kwa Ife–Iye adzabwezeretsanso miyoyo yathu mumpingo, ngati tichita zimene Mulungu akufuna.

5) Tikudikira chitsitsimutso koma chitsitsimutso chikutidikiranso. Chitsitsimutso chidzafika pamene tichita zimene Mulungu akufuna kwa Ife.

> *"ndipo anthu anga ochedwa padzina langa akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zawo zoipa; pamenepo ndidzamvera mmwamba, ndikukhululukira choipa chawo, ndikuchiritsa dziko lao."*

c. Mbali Yathu – ZOFUNIKIRA PA CHITSITSIMUTSO:

1) Akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga,

a) Kudzichepetsa kumatanthauza: kudalira; kudzitsitsa.

b) Uku ndi kudziyesa tokha kuti tili chabe ndikufuna nkhope ya Ambuye.

c) Anthu achipangano chakale adali ndi nthawi yakusala kudya ndi kupemphera podzichepetsa kwa Mulungu ndikupempha chisomo chake (Onani Masalimo 35:13 ndi Danieli 9:3).

d) Mpingo Wa Chipangano Chatsopano udakhala ndi nthawi yopemphera ndikusala kudya kupempha chifuniro cha Mulungu ndi mdalitso mmiyiyo yawo (Onani machitidwe 14:23).

Pamene tisala kudya timatanthauza kuti tikumufuna Iye kuposa zonse. Koma ngati tisala opanda kulapa ndiye kuti palibe chimene tachita.

2) Lapani: Tiyenera kusiya zimene sizimusangalatsa Mulungu, (njira zoipa).

a) Nenani zinthu zimene zikuchitika mdera komanso mumpingo koma Mulungu sakukondwera nazo. Mulape pa izi.

b) Kusala koyenera kumalimbikitsa kusiya machimo ndikuchita zimene Mulungu akufuna (Onani Yesaya 58). Fotokozani tanthauzo lachaputalachi.

4. Chitsanzo – A Charles Finney –Mlaliki wa ku Amelika amene Mulungu anamugwiritsa ntchito panthawi Yakutsitsimuka Kwakulu Pa Uzimu mzaka za mma 1900.

a. A Finney amalalikira ndi mphamvu yakudzoza kwa Mzimu Woyera.

1) Panthawi yamisonkhano yachitsitsimutso anthu amagwa paguwa potsusika ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ndikulapa poopa kuti angafe ngati salapa machimo.

2) Nthawi ina akuchitisa misonkhano ya chitsitsimutso nthawi yaku madzulo, adaganiza zokayendera fakitale ku kudera lina kuti akaone mmene makina amagwirira ntchito yake. Pamene mkulu wafakitale adamutengera pamakina ena, mayi wina anagwa akulira ngati akumva kupweteka, kenaka aliyense mufakitalemo adagwa nalira kwambiri ngati akumva kupweteka. Iwo adali kukhudzidwa ndi machimo awo. A Finney sadanene kanthu kalikonse. Koma kudzoza kudali kwamphamvu mmoyo mwawo mwakuti anthu adakhudzika ndi uchimo wawo. Mkulu wafakitale adamupempha Finney kuti ayankhule ndi anthu ake kuti amasulidwe ku uchimo wawo. A Finney adalalikira za Yesu ndipo aliyense mufakitalemo adamulandira Yesu ngati Mpulumutsi wake patsikulo.

b. Chinsinsi Chakupambana kwa A Finney.

1) A Charles Finney mumbiri yawo akuti padali munthu wina dzina lake Bambo Nash ndipo amakonda kuchititsa misonkhano ya Mawu a Mulungu mdera lawo ndipo amafika kuderalo nkudzakhala ndi nthawi yakusala kudya ndi kupemphera sabata ziwiri msonkhano usadayambe. Keneka amapeza anthu awiri ndikumapemphera nawo limodzi mderalo. A Nash ndi Akhristu othandizana nawo mpemphero amatha kusala kudya kupempha Mulungu kuti adzoze a Finney pamene akukalalikira mderalo. Mulungu amakhala ndi a Finney nthawi zonse pamene apemphera kolimba.

2) Mulungu amasunthika ndi pemphero ndi kusala kudya kwa a Nash kuposa ulaliki wa a Finney.

Kutsiliza: Kuitana kuti Tidzipereke

Mbusa akumbutse mpingo kufunikira kwa ulemerero wa Mulungu lero lino mumpingo wathu. Limbikitsani kuti mpingo ukhale ndi nthawi ya kusala kudya ndi kupemphera kuti chitsitsimutso cha chiyero chipezeke:

- Mumiyoyo yawo
- Mumabanja awo
- Pampingo wawo
- Mdera lawo
- Mumpingo wa Nazarene mu Afirika muno
- Gwiritsani ntchito kalendala yapemphero nthawi ino kupempherera afirika yense pazosowa zake komanso zosowa zampingo muno mu Afirika.

Mbusa Howie Shute